

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO KUPITA
KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

KODI INU MUNALANDIRA MZIMU WOYERA?


“Ndipo panali, pamene Apolo anali ku Korinto, Paulo anapita pa maiko a pamtunda, nafika ku Efeso, napeza akuphuzira ena; ndipo anati kwa iwo, Kodi munalandira Mzimu Woyera pamene munakhulupira?” (Machitidwe 19:1-2a).

Ophuzira a ku Efeso anakhulupirira za kutembenuka mtima koma samadziwa za dongosolo lonse la chipulumutso limene lippezeka mwa Yesu Khristu. Atamva za uthenga wabwino, iwo anabatizidwa. Paulo anasanjika manja pa iwo, napemphera, ndipo iwo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera.

Anthu ambiri anapempherako kuti machimo awo akhululukidwe ndi kulandira Khristu monga Mpulumutsi, koma sanayambe asangalalako ndi moyo weniweni wauzimu ndi wachigonjetso. Iwo sakhala ndi moyo wauzimu wozama ndi wolemerera umene umabweretsa chisangalalo. Ambiri amayamba bwino ndi Ambuye koma nthawi ikamapita amakumana ndi mayesero aakulu ndipo chifukwa cha ichi amabwerera m'mbuyo nkupitanso ku moyo wao wakale umene Mulungu anawapulumutsa. Kwa iwo amene sabwereranso ku moyo wa uchimo, ambiri a iwo amakhala ndi moyo wauzimu

wokwinimbira ndi wosakula komanso a chikhalidwe chongooneka ngati cha Umulungu.

Tangoganizani za wophuzira Petro, amene chadzulo lake lisanafike tsiku la



*“Mulungu afuna
kukupatsani mphatso
ya Mzimu Woyera.”*

Pentekoste anavomereza za kudzipereka kwake kwa Khristu. Iye anafika mpaka posolola lupanga lake, kukonzekera

nkhondo, pamene Yesu anagwidwa m'munda wa Getsemane. Koma patangopita maora ochepa, Petro yemweyo ananena katatu konse kuti samudziwa Ambuye wake. Pamene anayesedwa, pamene anakakamizidwa achite zimene anzake akufuna, kapena mu imfa imene, Petro analibe mphamvu zokhalirabe wokhulupirika. Koma pamene Mzimu Woyera anatsika pa tsiku la Pentekoste, Petro analalikira ndi mphamvu komanso kulimbika kwatsopano uthenga wonena za Ambuye woukitsidwayo. Iye anadzazidwa ndi mphamvu komanso zisomo za Mzimu Woyera. Sanabwereranso ku moyo wowedza nsomba koma anakhala moyo wachiyero ndi wodzikhuthula kwathunthu kwa Mulungu.

Uthenga wabwino ndiwo wakuti Mulungu akufuna kukupatsani mphatso ya Mzimu Woyera kuti mukhale ndi moyo wa mphamvu ndi chiyero chosasintha. Munthu aliyense payekha sangathe kukhala moyo wachiyero mwamphamvu kapena kuthekera kwake. Yesu anafa pa mtanda kuti machimo athu akhululukidwe kudzera mu mwazi wake wotetezera.

(Zapitirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi

Tsamba 3

Kusanthula Mau a
Mulungu: Kudzazidwa
ndi mzimu woyera

Tsamba 4

Nkhani yotsagana nayo:
Kudzazidwa ndi mzimu
woyera

Tsamba 5

Mafunso ndi Mayankho

Tsamba 7

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

Tsamba 8

zimene BAIBULO limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Pamene talapa, timatsukidwa ndi kukhala chipangizo choyera kudzera mwa Yesu Khristu. Tiyeni tisaleke kungokhala chipangizo choyera basi. Yesu anabwera kuti tidzazidwe ndi Mzimu Woyera. Ngati munthu wina sachita mwachangu pa kupempha Mulungu kuti amupatse Mzimu Woyera, mdierekezi adzayesetsa kudzazitsa moyo wathu ndi uchimo komanso zodetsa za dzikoli. Chidzalo cha Mzimu Woyera ndi chimene chimachiritsa wobwerera m'mbuyo ndi kumupangitsa kuti akhale ndi moyo wachiyero.

Yesu anabwera kudzakwaniritsa, ndi kumalizitsa ntchito yowapatsa anthu zowayenerenza kuti akhale ndi moyo womvera ndi wachiyero molingana ndi Mau a Mulungu. Iye anabwera kudzafufuta tchimo limene timachita kenaka ndi kutibatiza ndi Mzimu. Ndi chinthu chodabwitsa kwambiri kuti munthu akhale ndi chipulumutso chodzaza. Umenewu ndi moyo wodzipereka kwathunthu kwa Mulungu. Kumeneku ndiye kukhala ndi moyo weniweni wachigonjetso mnthawi ya mayesero, wachilimbikitsa mnthawi ya msautso, wamphamvu zogonjetsera mayesero, ndiponso wa mtendere pakati pa namondwe. Umabweretsa moto ndi moyo watsopano pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndicho chinthu chofunikira kwambiri pakati pa Akhristu okhulupirira masiku ano. Muli mphamvu mwa Mzimu Woyera kuti tikhale ndi moyo opanda uchimo mpaka pamene Ambuye adzabwerenso.

Kodi munalawako ndondomeko yathunthu, yokwanira ya chipulumutsoyi? Kodi munalandira Mzimu Woyera pamene munakhulupirira?

—mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoonadi za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawa amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maombedwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa *email*, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma *email* a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa m'dzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, 605 Bishops Ct., Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.us

Mau a Mkonzi



“Iye wokhulupirira Ine, monga chilembo chinati, Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda, kuturuka m'kati mwache. Koma ichi anati za Mzimu, amene iwo akukhulupirira Iye anati adzalandire; pakuti Mzimu panalibe pamenepo, chifukwa Yesu sanalemekezedwa panthawi pomwepo.” —Yohane 7:38-39

Tsinde la chipulumutso chathunthu lagona pa chidzalo cha Mzimu Woyera. Mzimu amabweretsa moyo ndi chisangalalo kwa iwo amene adzazidwa ndi chimwemwe cha kupezeka kwake. Ndi chinthu chodzabwitsa kwambiri pa moyo uno kuti Mzimu akhale mwa ife ngati kachisi wake wa pansu pano.

Mu kalata ya ulendo uno ya The Gospel Truth, ndikukamba nkhani ya ‘Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.’ Zinali zondivuta kuti ndilembe za mutu umenewu chifukwa ndi waukulu ndipo malo anali ochepe. Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi chinthu chimene chili chofunikira kuti chichitike pakati pa Akhristu. Pali zachithupithupi ndi zadziko zambiri zimene zimachitika pakati pa anthu amene amadzitcha akhristu. Mzimu Woyera angathe kukonza mavuto ambiri amene akupezeka m’miyoyo ya anthu ambiri lero lino, komanso ngakhale m’mabanja ndi m’ mipingo.

Mphatso iyi ya Mulungu ikunenedwa mmalo ambiri ngati: ntchito yachiwiri ya chisomo, kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, kubatizidwa ndi Mzimu Woyera, kuyeretsewa, kukonzedwanso, etc. Ndi zomvetsa chisoni kuti pali chisokonezo chambiri pokhudzana ndi chiphunzitso chimenechi. Pali miga-wano ndi mipatuko yambiri imene yachitika mu thupi la Khristu chifukwa cha nkhani imeneyi. Ifeyo sityenera kulola kuti ziganizo ndi malingaliro ongopeka a munthu alamulire choonadi, koma kuti Mau a Mulungu atsogolere kumvetsetsa kwathu. Pamene kuli kofunikira kuti timvetsetse chiphunzitso choona ndi chenicheni pa nkhanayi, kofunikira kwambiri ndiko kwakuti tidzazidwedi ndi Mzimu Woyera.

Nkhani imeneyi si yovuta kapena yosokonekera monga mmene mdaniyo wayipangira kuti idziwon-ekera. Yesutu analankhula momveka bwino za Mzimu Woyera kuti ndi amene amabweretsa mphamvu pa moyo wathu. Pa nkhani imeneyi, malemba amakhazikika pa mfundo yakuti Mulungu ndi amene amapereka mphatsoyi kwa okhulupirira kuti iwapangitse kuti akhale olimba, iwatonthoze ndi kuwatsogolera. Mau a Mulungu amanenetsa kuti kudzazidwa ndi Mzimu kumachitika pamene munthu walungamitsidwa. Pali kuopsa pamene tiphatikiza ziwirizi ngati chimodzi, komanso pali kuopsa pamene tizilekanitsira kutali ngati zinthu ziwiri zosiyana kwambiri mwakuti anthu saonanso phindu ndi kufunikira kwake kolandira Mzimu Woyera pamene alungamitsidwa. Ntchito zonse ziwirizi zinabwera kudzera mu nsembe ndi dongosolo la Yesu Khristu.

Anthu ambiri masiku ano akusowa mphamvu ndi moto pa zochitika zawo. Ineyo ndikhoza kuchitira umboni za mphamvu yodabwitsa ya Mzimu imene imayeretsa, imalimbisa, imapereka kuthekera ndi kutipangitsa kuti tikhale odekha. Ngati simunalandire Mzimu Woyera, ino ndi nthawi yabwino ndi yopambana kuti mupemphere ndi wina wake kuti nanunso mulandire nawo chidzalo chimenechi kuti kudzera mwa Mzimu mukhale m’ moyo wokondweretsa Mulungu.

Michael W. Smith

April 2014

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.us

kuti mudzilandira

makalata athu kapenanso

kuti muone makalata

akale.

Pamene tiyenera kufunafuna



Mzimu Woyera

Akhristu ambiri amachedwa kufunafuna kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Nthawi zambiri iwo amadikira nthawi yaitali ndipo amataya chikhulupiriro chawo chifukwa chosowa mphamvu m'moyo wao.

Baibulo silinena kuti tidikire nthawi yaitali bwanji kuchokera pamene tala-pa kufika pamene tikufunafuna Mzimu Woyera, koma monga mwa zitsanzo zimene zaperekedwa, ndikoyenera kuti munthu amene wakhulupirira kumene afunefune Mzimu Woyera mwachangu.

Yesu sanafune kuti ophunzira ake akumane ndi zochitika m'dziko ali osakonzekera, choncho anati: "Khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba" (Luka 24:49). Paulo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera m'masiku ochepa chabe atangotembenuka mtima. Pamene anthu ena a ku Samariya anavomereza Khristu, nthawi yomweyo ophunzira aja anatumiza munthu kwa iwo ndi uthenga wa Mzimu Woyera.

Pali kuopsa kwakukulu pamene tichedwa. Pamene munthu amene walungamitsidwa ndipo wazindikira chosowa chake, imeneyo ndiye nthawi yoyenera kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.

KALAZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: KUDZAZIDWA NDI MZIMU WOYERA

Kuwerenga Mau a Mulungu: *Ndipo pakufika tsiku la Pentekoste, anali onse pamodzi pa malo amodzi. Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ochokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzaza nyumba yonse imene analikukhalamo. Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha wayekha. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera....* —Machitidwe 2:1-4a

Kuumba mkota: Yesu anafa kuti apulumutse anthu ku machimo awo ndiponso kutipatsa chidzalo cha Mzimu Woyera. Mzimu Woyera amapatsa wokhulupirira zoyenerera kuti akhale ndi moyo wachiyo kudzera mu mphamvu, utsogoleri ndi chilimbikitso kuchokera kumwamba.

I. Ulosi wa Mzimu Woyera

- A. Yoweli 2:28-29 Mulungu adzatsanulira Mzimu Wake.
- B. Ezekiele 36:26-27 Mulungu amaika Mzimu Wake mkati mwathu.

II. Mzimu Woyera Alonjzedwa

- A. Mateyu 3:11 Yesu adzakubatzani ndi Mzimu.
- B. Yohane 14:16 Mulungu adzapereka.
- C. Luka 24:49 Yesu adzatumiza.
- D. Machitidwe 1:4-5 Dikirani lonjezo.

III. Kachisi wa Mzimu Woyera

- A. Machitidwe 7:44-49 Chihema/Kachisi wa mu Chipangano Chakale.
- B. 1 Akorinto 3:16-17 Inu ndinu kachisi wa Mulungu.

IV. Mzimu Woyera ndi Mphatso ya anthu Onse

- A. Machitidwe 2:38-39 Kwa inu ndi ana anu.
- B. Machitidwe 10:45 Ayuda ndi Amitundu.

V. Zofunikira kuti mubatizidwe ndi Mzimu Woyera

- A. Machitidwe 2:38 Lapani.
- B. Machitidwe 19:2 Khulupirirani.
- C. Machitidwe 5:32 Mverani.
- D. Aroma 12:1-2 Kupatulidwa.

VI. Mzimu Woyera apereka kwa iwo okha amene alungamitsidwa

- A. Machitidwe 8:5-6, 12-17 Mpingo wa ku Samariya.

- B. Machitidwe 9:17 Mtumwi Paulo.
- C. Machitidwe 10:1-2, 44-47 Nyumba ya Kornelio.
- D. Machitidwe 19:1-7 Ophunzira ku Efeso.

VII. Ntchito ya Mzimu Woyera

- A. Machitidwe 1:8 Amapereka mphamvu, Amatipatsa kuthekera.
- B. Aroma 15:16 Kupatula.
- C. Machitidwe 15:8-9 Kuyereza.
- D. Yohane 14:26 Kutonthoza, Kuphunzitsa.
- E. Yohane 16:13 Kutsogolera.
- F. Aefeso 1:13 Kupereka chikole.
- G. 2 Akorinto 3:6 Amapereka moyo.
- H. 1 Akorinto 12:4-11 Mphatso za Mzimu.
- I. Aroma 5:5 Amaika chikondi mu mtima mwathu.
- J. Ahebri 2:11 Kuyanjanitsa.

VIII. Zitsimikizo za Mzimu Woyera

- A. Aroma 8:16 Mzimu mwini.
- B. Agalatiya 5:22-25 Chipatso cha Mzimu.
- C. Aroma 14:17 Ufumu wa Mulungu.

Mau Omaliza

Ndipo ndani wa inu ali atate, mwana wache akadzampempha mkate, adzapatsa mwala? Kapena nsomba, nadzamninkha njoka mmalo mwa nsomba? kapena akadzampempha dzira kodi adzapatsa chinkhanira? Poto, ngati inu, okhala oipa, mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, koposa kotani nanga Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo akumpempha lye? Luka 11:11-13

KUDZAZIDWA NDI MZIMU WOYERA

Nkhani yothandizira posanthula Mau a Mulungu

MZIMU WOYERA APEREKEDWA

Pa tsiku la Pentekoste, Mzimu Woyera anatsika kuchokera kumwamba (Machitidwe 2:1-4) nadzaza mitima ya okhulupirira amene analipo 120. Okhulupirira amenewo anali oyamba mu mpingo wa Chipangano Chatsopano kuona ndi kulandira chidzalo chonse cha ndondomeko ya Mulungu imene anayikwaniritsa kudzera mwa Yesu Khristu. Mu nthawi ya mafano ndi chipembedzo chabodza chodzaza ndi uchimo komanso kulephera ku uzimu, Yesu anabweretsa chipulumutso ku dziko lapansi kuti mtundu wa anthu ukakhale m'moyo wa chigonjetso ndi wachiyero kudzera mu mwazi woombola ndi mwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

LONJEZO LA ATATE

Tikayang'ana kutsogolo ku nthawi ya Pentekoste, Mulungu analengeza zolinga zake pa Ezekiele 36:27: "Ndipo ndidzaika mzimu wanga m'kati mwanu, ndi kukuyendetsani m'malemba anga; ndipo mudzasunga maweruzo anga ndi *kuwachita*." Panalibenso zakuti munthu amangike ndi kukokeka ku chisalungamo, koma kuti Mulungu anapereka za iye yekha kudzera Mzimu wake kuti pakutero munthu akhale m'moyo wachiyero pakati pa dziko limene liri lauchimo. Kenaka Mulungu ananenanso za tsiku lija pamene anati: "ndidzatsanulira mzimu wanga pa anthu onse," (Yoweli 2:28).

MALO AMENE IYE AMAKHALA

Mu Chipangano Chakale, Mulungu amapezeka ndi kuyanjana ndi munthu poyamba mu chihema chokomanacho kenaka mu kachisi. Izi zinali nyumba zomangidwa ndi manja a anthu. "Komatu Wamwambamwambayo sakhala m'nyumba zomangidwa ndi manja; monga mneneri anena, ... Mudzandimangira nyumba yotani? Ati Ambuye; Kapena malo a mpumulo wanga ndi otani?" (Machitidwe 7:48-49). Funso limeneli likuyankhidwa pa 1 Akorinto 3:16-17. "Kodi simudziwa kuti muli kachisi wa Mulungu, ndi *kuti* Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu? Ngati wina aononga kachisi wa Mulungu, ameneyo Mulungu adzamuononga; pakuti *kachisi* wa Mulungu

ali wopatulika, ameneyo ndi inu." Mulungu amakhala mmalo oyera okhaokha ndipo chomwecho Mzimu Wake sangakhale mu kachisi wa thupi lathuli pokhapokha litayeretsedwa ku uchimo kudzera mwa Yesu Khristu.

YESU ANABWERA KUDZAKONZA NJIRA YA MZIMU

Yohane Mbatizi anaona Yesu ndipo analankhula za ubatizo wa Mzimu Woyera umene udzabwere. "Inetu ndikubatzani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima; koma ...lyeyu adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera *ndi moto*" (Mateyu 3:11). Yesu anabwera kudzakonza njira pa kubwera kwa Mzimu Woyera. "Ndipo onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba" (Luka 24:49). Lonjezo la Atate likunena za mphatso ya Mzimu Woyera.

APEREKEDWA KWA ONSE

Mphatso iyi yodabwitsa kudzera mwa Mzimu Woyera inaperekedwa poyamba pa tsiku la Pentekoste kwa Ayuda okhulupirira, koma inalonjezedwa kwa anthu onse a mibadwo ilinkudza. "Pakuti lonjezano liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa onse akutali ..." (Machitidwe 2:39). Mzimu Woyera anaperekedwa osati kwa Ayuda okha komanso kwa Amitundu. "Ndipo anadabwa okhulupirirawo akumdulidwe onse amene anadza ndi Petro, chifukwa pa amitundunso panathiridwa mphatso ya Mzimu Woyera" (Machitidwe 10:45). Ngakhale dzikoli liyipe motani, Mzimu Woyera amapezekabe kwa okhulupirira.

Anthu ena amaganiza kuti ayenera kuchita chinachake kuti akhale ndi Mzimu Woyera kapena kupemphera kwambiri kuti poteropo Mulungu akhoza kuwayankha. Sichoncho, iyi ndi mphatso imene imaperekedwa mwaulere ngati zinthu zoyenerera zakwaniritsidwa.

(Zapitirira pa tsamba 6)



Lonjezo la Atate

*"Komatu mudzalandira
mphamvu, Mzimu Woyera
atadza pa inu."
Machitidwe 1:8*

(Kuchokera pa tsamba 5)

CHIMENE MUNGACHITE KUTI MULANDIRE MZIMU

Kodi nanga munthu achite chiyani kuti alandire Mzimu Woyera? “Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera” (Machitidwe 2:38). Mzimu Woyera adzabwera m'moyo wa munthu pokhapokha iye walapa kaye machimo ake. Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumachitika mwa chikhulupiriro ndipo kumaperekedwa kwa iwo amene akhulupirira mwa Khristu (Machitidwe 19:2) ndipo akukhala m'moyo womvera Mulungu (Machitidwe 5:32). Mzimu amadzaza mu mtima umene uli woyera, choncho lye adzabatiza moyo okhawa umene wadzipereka kwathunthu kwa Mulungu. “Chifukwa chache ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, *ndiko* kupembedza kwanu koyenera” (Aroma 12:1). Mu Chipangano Chakale, moto umapsereza nsembe zimene zimayikidwa pa guwa, chomwechonso ndi Mzimu Woyera, amene amafanizidwa ndi moto, adzafika pa munthu yekhayo amene wadzipereka kwathunthu ku chifuniro ndi cholinga cha Mulungu. Lapani, khulupirirani, mverani, ndipo mudzikhuthule kwathunthu ndipo Mulungu adzakubatzani ndi Mzimu Woyera.

PALI NTCHITO ZIWIRI ZOSIYANA

Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi ntchito yapayokha ndi yapadera imene isiyana ndi zimene zimachitika munthu akalungamitsiwa. Pali Malemba awiri amene tawaona kale amene akugwirizana ndi mfundo imeneyi ya ntchito yochitika kawiri ya chipulumutso monga mmene tikuonera mu zitsanzo zonse za Mpingo wa Atumwi zimene zaperekedwa mu buku la Machitidwe. Filipino analalikira za Yesu kwa anthu a ku Samariya. Ambiri mwa iwo analandira Yesu ndipo anabatizika. Kenaka Petro ndi Yohane anabwera ku Samariya kudzawapempherera anthuwo kuti “alandire Mzimu Woyera” (Machitidwe 8:15). Mulungu anawapulumutsa ku uchimo kenaka anawadzaza iwo ndi Mzimu Wake. Mbale Saulo, amene dzina lake lina sinthidwa kukhala Paulo,

Mzimu Woyera

Amatipatsa mphamvu pa nthawi imene tafooka,

Chisomo pa nthawi imene tayesedwa,

Ndi chigonjetsa pamene tikufuna kugonjetsedwa.

analandira Khristu ndipo kenaka analandira Mzimu Woyera kudzera mu mapemphero a Hananiya. Chimodzimodzinso, akhristu ena, monga tikuonera mnyumba ya Kornelio (Machitidwe 10) ndi ophuzira a ku Efeso (Machitidwe 19), anadzazidwa ndi Mzimu Woyera panthawi zosiyana kuchokera pamene anatembenuka mtima.

MZIMU WOYERA AMABWERETSA MPHAMVU ZOGONJESERA

Mzimu Woyera amachita zinthu zambiri ndipo amasintha kwathunthu moyo wa munthu amene watembenuka mtima. Chachikulu, m'mau a Khristu, Mzimu Woyera amapereka mphamvu – mphamvu kukhala moyo wopanda uchimo, mphamvu pa undekha ndi pa thupi lathu, mphamvu pa kukhala m'moyo wachiyero, mphamvu pa kukhala molingana ndi Mau a Mulungu. “Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ache a dziko” (Machitidwe 1:8). Mzimu Woyera amatipatsa mphamvu pa nthawi imene tafooka, chisomo pa nthawi imene tayesedwa, ndi chipambano pamene tikufuna kugonjetsedwa. Anthu olungamitsidwa “amayeretsedwa ndi Mzimu Woyera” (Aroma 15:16). Iwo amasankhidwa, napatulidwa, ndi kukhala oyera kudzera mu mphamvu ya Mulungu. Mitima yawo ndi yoyeretsedwa ndi Mzimu (Machitidwe 15:9). Kudzera mu mphamvu ya Mzimu, zikhumbitso za thupi zimamangidwa ndipo pamakhala kuthekera kochokera kumwamba kuti athe kunena kuti “ayi” kwa mdierekezi kapena “eya” kwa Mulungu.

NTCHITO ZINA ZA MZIMU WOYERA

Mzimu Woyera ndi mtonthozi ndi mphunzitsi (Yohane 14:26). Iye amatsogolera ndi kuwongolera anthu Ake. Mzimu Woyera amatsogolera ndiponso kupereka mphatso zauzimu (1 Akorinto 12:4-11). “Chikondi cha Mulungu chinatsanulidwa m’mitima mwathu mwa Mzimu Woyera.” (Aroma 5:5). Mzimu wa Mulungu amayanjanitsa anthu enieni a Mulungu (Ahebri 2:11). Mzimu Woyera amapereka moyo, changu ndiponso cholinga. “Chilembo chipha, koma mzimu uchititsa moyo” (2 Akorinto 3:6b). Pamakhala chiyamiko, chiyero ndi kupembedza kwenikweni m’miyoyo ya anthu amene adzazidwa ndi Mzimu Woyera.

CHITSIMIKIZO CHA MZIMU WOYERA

Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi ntchito ya chikhulupiriro ndipo nthawi zonse sizichitika ndi ziwonetsero zazikulu kapena mmene munthu akumvera. “Mzimu yekha achita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu” (Aroma 8:16). Aphunzitsi ambiri onyenga amanena kuti chitsimikizo cha Mzimu Woyera ndiko kulankhula chinenero chosadziwika, chakumwamba. Komatu

Malemba amaphunzitsa kuti chitsimikizo chenicheni cha Mzimu: “Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro” (Agalatiya 5:22-23). Chitsimikizo chenicheni cha Mzimu Woyera ndiko kuthekera ndiponso mphamvu yokhala moyo wachiyero.

LANDIRANI MZIMU WOYERA NDI KUKHALA WOGONJETA

Chidzalo ndi kulemera kwa Ufumu wa Mulungu ndiko chilungamo, mtendere ndi chimwemwe zimene zimachokera kwa Mzimu Woyera wokhala mwa ife (Aroma 14:17). Akhristu ambiri akuvutika ndi zimene zimawachitikira. Mitima yawo ndi yofuna kuchita chifuniro cha Mulungu koma matupi ali olefuka. Mzimu Woyera wokhala mwa ife ndiye yankho ku mavuto ambiri amene alipo m’miyoyo ya anthu ndi mipingo. Kudzera mu kudzichepetsa ndi chikhulupiriro, nkofunika kungowapempha Atate, ndipo iwo adzapereka mosavuta mphatso ya Mzimu Woyera kwa onse amene apempha (Luka 11:11-13).

—mws



Funso: Kodi munthu akati wadzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndiye kuti sakhalanso ndi zofooka za ku umunthu ndi kukumana ndi mayesero?

Yankho: Ayi. Na ngati tili mu moyo uno, tidzakhala ofooka ndi kukumana ndi mayesero a thupi. Koma kusiyana kwake ndiko kwakuti ndi Mzimu Woyera, pali mphamvu yaikulu ndi kuthereka kochokera kumwamba zotithandiza kuti tigonjetse mayeserowo. Mtumwi Paulo ananena pa 1 Akorinto 9:27: “koma ndipumpuntha thupi langa, ndipo ndiliyesa kapolo; kuti, kapena ngakhale ndalalikira kwa ena, ndingakhale wotayika ndekha.” Tiyenera tikhalebe akufa ku undekha ndi kudzipereka tokha kwa Mulungu. Ngati tilephera kupitirira

kudziperekabe kwa Ambuye, tikhoza kutaya chipulumutso chatu. M’ moyo uno, munthu adzakhala ndi kuthekera kwa kuchimwa chifukwa chakuti ali ndi mwayi wosankha. Munthu asanadzazidwe ndi Mzimu Woyera,



Kulani m’chisomo

ganizo lake limakhala lopendekekeru ku uchimo. Koma kenaka. Malingaliro ake amakhala oyang’ana ku chiyero chifukwa cha mphamvu yakuyeretsa ya Mzimu.

Tikakhala ndi Mzimu Woyera, timapatsidwa zotiyenereza kuti tipitirire pa moyo wauzimu ndi kukula mu zinthu

za Mulungu. “Koma kulani m’chisomo ndi chizindikiritsa cha Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Kristu” (2 Petro 3:18a). Nthawi zonse tidzakhala ndi magawo a umunthu wathu amene Mzimu Woyera akuwakonzanso. Anthu amene adzazidwa ndi Mzimu Woyera amakhala ndi moyo wapaderadera, komabe Mzimuyo amawabweretsa ku chikhulupiriro chofanana ndi cha Yesu Khristu. Moyo wofuna kudziwa cholinga komanso chifuniro cha Mulungu umakhlapobe. Munthu woyera mtima amene ali wake wa Mulungu akhoza ndipo amakhala ndi moyo wachiyero wopanda uchimo.

Anthu amatha kulakwitsa pamene ali pa ulendo uwu wokula mu uzimu, komabe mtima umakhala wolunjika ka Mulungu. Pamakhalabe magawo amene Mzimu amakhala akuwagwiritsa ntchito kuti atipangitse ife kuti tikulekulebe ndi kukhala wokhazikika pa moyo wauzimu.

—mws




KODI MUKUDZIWA?

Pamene ophunzira aja analankhula ndi ‘malilime ena’ iwo anadzidwa ndi Mzimu Woyera, iwo samalankhula chinenero chakumwamba ndi chosamveka. Iwo amalankhula ziyankhulo kapena zinenero za maiko ena. Popeza “yense anawamva alikulankhula m'chilankhulidwe chache cha iye yekha” (Machitidwe 2:6).



“Mphatso imeneyi ya malilime” inali yodabwitsa chifukwa ophunzira anali asanaphunzireko zinenero zimene iwo anazilankhula. Chimenechi chinathandizira kwambiri kufalitsa uthenga wabwino ndi kulimbikitsa mfundo yakuti chipulumutso ndi mphatso ya kwa anthu onse.



Sanayenda-yendanso ndi Iye

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA
Email:
editor@thegospeltruth.us

Pa ichi ambiri a akuphunzira ache anabwerera m'mbuyo, ndipo sanayenda-yendanso ndi Iye.
—Yohane 6:66

YESU, Mwana wodzozedwa wa Mulungu, anakumana ndi kukanidwa kwakukulu panthawi ya utumiki wake pa dziko lino. Ena a iwo sanangomulandira kokha, panalinsophunzira amene kanthawi kena adamutsatira ndi kumvera zophunzitsa zake koma kenaka amamutembenukira ndipo sanayendanso ndi Iye. Iwo sanafunenso kuyanjana naye kapena kuvomereza kuti Iye anali Mesiya.

Ambiri anakhumudwa ndi ziphunzitso za Uthenga wabwino. Popeza anali ndi maganizo a umunthu, sanali okonzeka kuunika miyoyo yawo ndi chiyero cha choonadi. Iwo sanali okonzeka kudzikana okha ndi kulola kutsatira Ambuye ndi mtima wao wonse. Kwa Yesu, izi zinali zopweteka kwambiri. Iye anasiya ulemmero wa Kumwamba nabwera pansipano, kudzipereka yekha chifukwa cha chikondi chake chachikulu.



CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Monga mmene zinaliri pa nthawi ya Khristu, momwemonso zili choncho ndi abusa enieni a uthenga wabwino a masiku ano. Padzakhala anthu amene adzakana utumiki wanu, kudzipereka kwawo kwathunthu ndiponso chikondi chanu. Iwo adzakhumudwa ndi choonadi ndipo ena sadzayanjana nanunso. Nthawi zambiri, anthu amanamizira mbusa kapena mpingo mmalo mongovomereza kuti akukana machitachita a Mulungu pa moyo wao. Izi zimabweretsa kupwetekedwa ndi kuwawidwa kwa mzimu kwa iye amene akuyang'anira nkhosaza Ambuye. Mukhale okhulupirika ndipo musatayirire pa choonadi chimene chili mwainu chifukwa chongofuna kuti mukope chigulu cha anthu. Lalikirani choonadi chonse modzichepetsa, mwachikondi ndi mchilungamo cha chiweruzo.

Mbale Ostis amakonda kunena kuti: “Ngati mukondweretsa Mulungu, mudzakondweretsa wina aliyense amene ayenera kukondweretsedwa.”

—mws